


File



# TANTHAUZO LA KUKHALA MKRISTU



# TANTHAUZO LA KUKHALA MKRISTU



# TANTHAUZO LA KUKHALA MKRISTU

YTn4
NYA

# TANTHAUZO

# LA

# KUKHALA

# MKRISTU

# WHAT IT MEANS TO BE A CHRISTIAN

*(Chinyanja)*

*Published by*
*Baptist Publishing House*
*P.O. Box 31995, 10101*
*Lusaka, Zambia*

*Printed by*
*Baptist Printing Ministry*
*P.O. Box 31995, 10101*
*Lusaka, Zambia*

cifukwa ca ici. Tiyenera kukhala kapolo wa abale athu, koma moyo woposa kotani kuposa kukhala ngati Mbuye wathu! Mu mphamvu ya Mulungu, mungakhale wa mkuru cifukwa mungakhale kapolo.

**MAFUNSO OKAMBIRANA:**

1. Kambiranani za anthu a m'Buku Lopatulika amene anali zoonadi akapolo. Kodi anacita ciani?
2. Kodi mungacite ciani tsiku lino la Ambuye monga kapolo?
3. Kodi muganizira Mulungu alankhula ciani za zicitidwe zina za bwino zimene zimacitidwa cifukwa cakuti muyenera kucita tero?



**Za Mkatimu**

**Mutu** **Tsamba**

1. Kodi Mkristu ndani? .............................. 5
2. Kodi Munthu Angakhale Bwanji Mkristu? ........... 8
3. Kodi Cipembedzo Coona ndi Citi? .................11
4. Kodi ndi Ngatumikire Mulungu Motani? ............14
5. Nanga za Cimo? ..................................17
6. Kodi Angakhale Membala wa Mpingo Ndani? .......21
7. Kodi Ndani Angakhale Mtumiki? ..................25
8. Kodi Angakhale Mbusa Ndani? ....................29
9. Kodi Munthu Angayambe Mpingo Motani? ..........32
10. Kodi ndi Cifukwa Ciani Ndiyenera Kupereka ca Khumi? ...................................36
11. Kodi Ndingagawire Bwanji Cikhulupiriro Canga? .....39
12. Kodi Angakhale wa Mkuru Ndani? ................43

ndi mizimu ya anthu. Mungakhale ndi mphatso ya kuthandiza anthu ndi mabvuto awo, kumvera ku zocititsa ena mantha ndi mabvuto ndi kuwathandiza kuyagonjetsa. Kodi anthu kawiri-kawiri amabweretsa mabvuto awo kwa inu? Ngati ndi tero Mulungu wakupatsani inu nchito yaikulu. Mungakhale kapolo woona kwa iwo. Mungakhale wociritsa cifukwa anthu onse afuna wina wolankhula naye. Munthu amene angaciritse mzimu wobvutika angalodzere obvutika ku mfumu ya mtendere.

Mulungu afuna atsogoleri. Afuna iwo amene apatsa ena ciyembekezo, anthu ali ndi colinga cimene amacititsa ena kugwira nchito ndi kutsatira. Wina ayenera kunyamula katundu wa udindo wa kuthetsa mabvuto monga mtsogoleri. Ndiponso payenera kukhala a nchito okhulupirika. Kapena simungakhoze kulankhula kapena kuphunzitsa kapena kuciritsa. Mungagwirire nchito Mulungu. Si zimene muli nazo koma zimene mucitira Mulungu ndiye zimene zifunika. Mulungu anakupatsani inu mphatso zimene mungagwiritse nchito kuthandiza ena. Adzakupatsani cikondi cace ndi mphamvu yace. Simunganene kuti palibe cimene mungacite. Anthu ali kuyembekezera ena kutenga nthawi ya kusamalira iwo. Mungakhale akuru cifukwa Yesu anaphunzitsa kuti kapolo ndiye wa mkuru pa onse. Ife tonse tingakhale akapolo. Mulungu adzakuonetsani zimene mungamucitire iye. Funso ndi lakuti kodi mudzacicita?

## 111. MPHAMVU YA MULUNGU LIMADZETSA UKURU

Yona ali cimodzi-modzi monga inu ndi ine. Sanafune kutsatira lamulo la Mulungu. Anaopa. Anadana nao anthu a ku Ninive, koma Mulungu anamcitisa kuti apite ndi ku kalalikira kwa iwo. Motero Yona anapita ndi ku kalalikira ciononngeko ndi ciweruzo. Sanakonde athu. Analalikira cifukwa anakakamizidwa kucita tero. Pambuyo pace anacoka, komatu anthu anatsutsidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Anapempha cikhululukiro. Mudzi wonse unatembenuka kutsata Mulungu cifukwa munthu analalikira mu mphamvu ya Mulungu. Ngati Mulungu akanagwiritsa nchito munthu wodzala ndi cidani monga Yona, kodi sangalandire mphatso zanu ndi kuthandiza ena? Kodi mudzakhala akuru? Ndiye kuti muyenera kukhala akapolo. Yesu anati sanadze kudzatumikiridwa koma kutumikira. Ukuru wace upezeka mu cikondi cace ndi kudzipereka nsembe cifukwa ca ife. Aliyense afuna kukhala wa mkuru, ndi Mulungu afunanso ife kukhala akuru. Ndi mphamvu zace m'kati mwa anthu wamba zimene zimadzetsa ukuru weni-weni. Komatu, tiyenera kulipira malipiro

wina wa mwamuna. Kapena mzimai anali cimodzi-modzi monga khalidwe la cikondi kwa Mulungu mwini.

Munthu amene ali wa mkuru nthawi zina sangakhale wochuka. Sangakhale wa cuma. Sangakhale wocenjera, koma adzakhala munthu amene agwiritsa nchito zimene Mulungu anampatsa kutumikira ena. Adzakhala bwenzi la ofuna thandizo ndi wotonthoza iwo ali ndi cisoni. Zicitidwe zace zingakhale zocepa, koma zidzakhala zoonadi za zikulu. Simuyenera kuti mucite zinthu za zikulu kuti mukhale akuru. Zinthu zocepetsetsa zocitika m'cikondi ndi zoposa wothamanga liwiro koposa kapena wopambana pa nkhondo. Mu 1 Akorinto 13 tiwerenga kuti palibe cimene ticita ciri ndi malo kwa Mulungu pokhapo citacitika mu cikondi. Macitidwe anu ocepa kwa munthu wina ndiye zokha zomwe ali nazo kuthandiza ena.

11. **KODI MPHATSO ZANU NDI ZOTANI?** 1 Akorinto 12:4-12

Kodi ndi ciani cimene Mulungu wakupatsani cimene mungagwiritse nchito pa kuthandizira ena? Ngati mufuna kukhala wa mkuru, muyenera kugwiritsa nchito zinthu izi ku za Mulungu ndi anthu onse. Malembo a phunziroli alankhula pa za mphatso zimene Mulungu wapatsa ku anthu. Tidzayang'ana pa zina za izo:

Kodi mungalankhule pa maso pa anthu? Kapena mungalankhule mu njira yokondweretsa ndi yokopa mtima. Munthu amene angacititse ena kumva monga iye amvera ndi kulamulira zicitidwe zao ndi mau ali ndi mphamvu zodabwitsa. Iyi ndi mphatso imene ingacite zabwino zambiri, koma ingaonongenso kwa kukulu. Ngati Mulungu wakupatsani inu luso la kulankhula, pomwepo lankhulani za iye. Mungalodzere ena kwa Mulungu ndi zimene mulankhula. Mbusa wa Cikristu, wa ndale, kapena mphunzitsi angacitire Mulungu zambiri. Kapena mungaphunzitse. Kodi mungaike zobvuta kumveka mu kalankhulidwe komveka bwino? Yesu anali m'modzi wa a ziphunzitsi odziwa kuphunzitsa bwino. Anali kucititsa anthu kufuna kuphunzira. Anagwiritsa nchito nzeru zace ndi kulodzera anthu ku njira yoyenera. Kuphunzitsa Mau a Mulungu ndi mphatso yaikulu. Kuti ukhale mphunzitsi wabwino uyenera kukonda anthu ndi kufuna kuwathandiza. Kodi muli mphunzitsi? Iwo amene ali odwala afuna wina wa kuwathandiza. Afuna wina amene angawaciritse. Ophunzira amacita zizindikiro za kuciritsa matupi a anthu. Mungakhoze kucita ici, kapena kupambanapo mungakhale wociritsa maganizo





## KODI MKRISTU NDANI?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Yohane 3:1-21

**MAU A PA MTIMA:** *"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana Wace Wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha."*
Yohane 3:16

Kodi Mkristu ndani? Kodi muganizira kuti mudziwa yankho? Ngati iai, bukuli lalembedwa ku kuthandizani. Mwa ilo, tidzayesa kuyankha mafunso amene mungakhale mufunsa pa za umoyo wa Cikristu.

### WOKHULUPIRIRA MWA KRISTU

Coyamba, Mkristu ndi wokhulupirira mwa Yesu Kristu. Ici citanthauza kuti omvetsetsa Yesu ndi ndani, ndi kubvomereza Yesu monga Mpulumutsi wa moyo wace. "Koma yembekezerani" mungafunse, "Kodi Yesu ndani?" Timaphunzira za Yesu mu Buku Lopatulika. Buku Lopatulika limatiuza za nkhani ya Mulungu, ndi cikondi ca Mulungu ca dzikoli. Mulungu anapanga dziko ndi kulenga zinthu zonse ziri momwemo (Genesis 1:1), koma sanaipange yopanda colinga. Anaipanga kuti ikakhale malo okhalapo munthu. Pomwepo anapanga munthu ndi kumuika mu dziko. Mulungu anali wopanda bwenzi, ndipo anafuna munthu akhale bwenzi lace. Koma mdani wa zonse zimene ziri zabwino, Satana, anabweretsa cimo mu dziko, ndipo munthu anasankha kukonda cimo koposa Mulungu. Ici cinabweretsa mpatuko wa ukulu pakati pa munthu ndi Mulungu, mpatuko umene Mulungu yekha anganthetse.

Mtundu wa Israyeli, mtundu wa anthu amene timacha Ayuda masiku ano, unali mtundu umene Mulungu anadzionetserako yekha. Anasankha Abrahamu (Genesis 12:1), tate wa Ayuda, ndi kuwadalitsa. Analankhula kwa onse mu citsamba coyaka moto, koma cosanyeka citsambaco (Eksodo 3), ndi pambuyo pace nampatsa malamulo khumi (Eksodo 20). Mu mbiri yonse ya Ayuda, analankhula ku anthu ace mwa aneneri ace, ndi kuwakonzekeratu za kudza kwa Yesu, mwana wace yekha, amene adzathetsa mpatuko wa ukulu pakati pa munthu ndi Mulungu mwa kacitidwe ka cikondi ca cikulu.

Yesu anapacikidwa. Anakhomedwa pa mtanda mpaka anafa. Anali mwana wa Mulungu, ndipo sanacimwepo. Komatu, analola yekha kuphedwa cifukwa ca anthu onse. Ngakhale Mulungu atikonda, koma ndikhalidwe la Mulungu kudana nalo cimo. Mphoto ya ucimo ndi imfa (Aroma 3:23). Koma Mulungu anatikonda ife kwambiri kotero kuti anatuma Yesu, mwana wace yekha, kutipulumutsa ife. Ngati tikhulupirira kuti Yesu anadza kutipulumutsa ife, monga Buku Lopatulika linenera, ndipo ife tilandira cipulumutsoco, Mulungu sationanso ife monga ocimwa.

Mulungu wapatsa yense wa ife danga lakuthetsa mpatuko pakati pa ife ndi iye. Koma tiyenera kukumana naye pakati. Tiyenera kubvomereza Yesu monga Mpulumutsi wa moyo wathu ndipo pamene ticita cotere, tikhala Akristu.

## KODI NDI CIFUKWA CIANI TIFUNIKA KUPULUMUTSIDWA?

Coyamba, Mulungu atipulumutsa ife kuti tikakhale ndi iye kwa muyaya. Kumbukirani tanena kuti Mulungu analenga munthu kuti ife tikhale abwenzi ace. Mulungu akhala kwa muyaya, ndi abwenzi a Mulungu akhalanso ndi moyo kwa muyaya. Anatipulumutsanso kuti timtumikire iye, pa dziko lapansi pano pomwe tikali ndi moyo mu thupi ndiponso kumwamba kwa muyaya ndi iye. Ici cititsogolera ku pfundo yathu ya ciwiri pa kumvetsetsa Mkristu ndani.

## YESU NDI AMBUYE

Siciri cokwanira kwa Mkristu kubvomereza cabe Yesu monga Mpulumutsi. Ayeneranso kulola Yesu kukhala Mbuye wa Moyo wace. Kodi amene alamulira moyo wanu ndani? Kodi mudziwa kuti Buku Lopatulika likuti Yesu afuna kukhala wolamulira mu miyoyo yanu. Ngati simulola yesu kulamulira moyo wanu, pomwepo Satana adzakhala ali kulamulira m' malo mwace. Yesu yekha ndiye angakhoze kucotsa cimo. Koma sangacite ici pokhapo mutamulola kutero. Ngati Yesu ndi Mpulumutsi wanu, koma sali Mbuye, muli kutaya madalitso ambiri amene Mulungu walonjeza:

1. Analonjeza kukhala ndi ife nthawi zonse. Koma ngati Satana akali kulamulira miyoyo yathu sitingakhoze kumva zimene Mulungu ali kunena.

2. Anatilonjeza ife mtendere mu miyoyo yathu koma sikungakhale mtendere uli wonse kumene kuli cimo. Cimo ndi





## KODI ANGAKHALE WA MKURU NDANI?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Yona 4:1-11; Mateyu 25:31-40; 1 Akorinto 12:4-21

**MAU A PA MTIMA:** *"Ndipo mfumuyo idzayankha nidzati kwa iwo, indetu ndinena kwa inu, cifukwa munacitira ici m' modzi wa abale anga, ngakhale ang' ono ang' ono awa, munandicitira ici ine."*
Mateyu 25:40

Mai wao wa Yakobo ndi Yohane anafuna zabwino koposa za ana ace monga mai aliyense wabwino angafune. Mu mutu 20 wa Mateyu, tiona momwe mai uyu anafunsira Yesu kupatsa ulemu ku ana ace. Anthu ambiri anaganizira kuti Yesu adzaikiza ulamuliro wace. Anali kufunitsitsa kuti alande ulamuliro wa Ciroma mwa upandu ndi kuikiza ulamuliro wa ufulu wa Cihebri. Mai uyu anali kufuna ana ace kuti akhale ndi maudindo akulu mu ulamuliro uwu. Anafuna kuti ana ace akhale akuru. Ophunzira ena sanagwirizane nazo izi, kapena cifukwa cakuti naonso anali kufuna malo amodzi-modzi. Yesu anagwiritsa nchito mpatawu kuwaphunzitsa phunziro lofunikira kwambiri. Ananena kuti iwo amene anali kufuna kukhala wa mkuru ayenera kukhala kapolo. Uku kunali kumasulira kwatsopano kwa ukuru. Ili likali phunziro lalikulu kwa ife lero cifukwa munthu aliyense angakhale wa mkuru.

**SICIYENERA KUKHALA CACIKURU** Mateyu 25:31-40

Ganizirani za munthu wa mkuru. Ngati mutachula anthu ambiri akuru-akuru kodi angakhale otani? Kapena munali mwaganizira za anthu ochuka andale, aphunzitsi, awiriwo. Timanena iwo kuti akuru cifukwa angacite bwino zinthu zina. Ali odziwa kulankhula bwino, kapena atsogoleri abwino. Angathamange kwambiri kapena anali a mphamvu koposa ena. Kodi kukhala wa mkuru ndiye kuti, uyenera kucita cinthu copambana kapena ca cikuru? Buku Lopatulika siliri tero! Anthu ambiri amene tingache akuru sali zoonadi akuru pamaso pa Mulungu. Mutu 25 wa Mateyu uli ndi fanizo la ciweruzo. Kodi anathandizira mbale wao pamene ali wodwala, kapena ndi njala, kapena m' ndende, kapena pa ulendo? Ndi zicitidwe zocepa zotere za cikondi zimene zinatanthauza ukuru kwa Mulungu. Iye mwini anauza za cifundo kwa munthu

Timapeza cipulumutso kupyolera mu kucita mwa cikhulupiriro. Cibwera mwa kukhulupirira. Simungatsimikizire. Mungakhulupirire cabe.


Ndime izi sizokhazo zimene ziri za phindu. Njira izi sindizo njira zokha. Kuli umboni wa padera umene mungapatse ndiye wa inu nokha. Cimodzi-modzi monga anthu ali osiyana, njira zao za kucitira umboni ziri zosiyana. Zothandizira izi zingakutsogolereni inu, koma muyenera kupeza njira ya Mulungu. Coyamba, mudziweni mu mtima wanu monga Mbuye ndi Mpulumutsi. Fufuzani ndi kupeza umboni wanu. Ife tonse ndife osiyana, koma ndife amodzi mwa Kristu. Ife tonse tingafikire ena kuti adze kwa Kristu ndi kuona.



yoipa, mtendere ndi wabwino, cabwino ndi coipa sizingakhale pamodzi.

Kuti mulandire madalitso onse amene Mulungu analonjeza, tiyenera kupanga Yesu Mbuye wathu. Pali njira zisanu za kupanga Yesu Mbuye zimene tidzakambirana mu mitu yotsatira. Awa ndi kutumikira Mulungu pa kuphunzira za iye; kutumikira Mulungu pa kubatizidwa; kutumikira Mulungu pa kukhala ciwalo ca mpingo; kutumikira Mulungu pa kugawira cikhulupiriro cathu; kutumikira Mulungu pa kugawira zimene tiri nazo. Ngati titatumikira Mulungu mu njira zonse izi ndi cikondi, pomwepo tinganene zoonadi kuti tapanga Yesu Mbuye wa moyo wathu.

Ici, apa, ciyankha funso lathu loyamba "Kodi Mkristu ndi ndani?" Mkristu ndi munthu aliyense, mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, amene wabvomereza Yesu Kristu monga Mpulumutsi ndi kumpanga Mbuye.



Mulungu anapatsa Mwana wace Yesu kuti mwa Iye anthu apulumutsidwe.

## KODI MUNTHU ANGAKHALE BWANJI MKRISTU?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Aroma 10

**MAU A PA MTIMA:** *"Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka."*

Aroma 10:9

Mu phunziro latha tinakambirana za funso "Kodi Mkristu ndani?" Mu phunziro lino tidzakambirana za funso, "Kodi munthu angakhale bwanji Mkristu?" Monga momwe tinanenera kale, munthu amakhala Mkristu pa kubvomereza Kristu monga Mpulumutsi. Kodi ici citanthauza ciani?

**YESU AMATIPULUMUTSA IFE**

Panali mulimi amene anali ndi malo akulu olimapo. Tsiku lina anabvutika. Anthu anapitiriza kudza ku malo ace kudula mitengo kupanga nkhuni. Anayesa njira zambiri zoletsa anthu. Anamanga linga. Analowetsa nchito amalonda. Palibe cimene cinaoneka monga cigwira nchito. Pomwepo tsiku lina pamene anali kusaka nyama ndi abwenzi ace anaganizira za msampha. Anakumba dzenje lalitali, ndi kuphimbapo ndi mitengo ndi udzu kotero kuti panaoneka monga polimba. Pomwepo anasegula cipata cace ndi kucotsa amalonda ace ndi kuyembekezera kuona comwe cidzacitika. Posacedwa guru la azimai linadza kudzaba nkhuni ku malo ace. Ataunjika mitolo ikulu-ikulu ayamba kucoka, koma mwadzidzidzi anaponda pa dzenje ndipo anagwidwa. Mulimi anamva kulira kwao ndipo anatenga cingwe kupita ku dzenje. Komweko anati, "Ndinali kufuna cabe ku kuphunzitsani phunziro, motero musadere nkhawa pa za cilango canga. Ndidzagwetsa cingwe, m'modzi ndi m'modzi ndidzakukokani ku kucotsani mudzenje. Koma sindingakukokeni inu pamodzi ndi mitolo ya nkhuni zimene mwaba. Muyenera kusiya mitolo yanu pansi pomwepo. M'modzi-m'modzi anawacotsa onse koma m'modzi amene anakana kusiya mtolo wace. Sudzamucitira cabwino, pansi paja; ndipo ngati atasiyidwa ndi mu dzenje adzafa ndi njala, koma anaumilira kumtenga.

Kodi iyi nkhani ifanidzidwa bwanji ndi Yesu? Ici cokha. Ciri ngati anthu onse agwera mu dzenje. Iyi ndi dzenje la ucimo, ndi umoyo wathu wa ucimo uli ngati mitolo ya nkhuni yakuba. Yesu ali ngati



kwa Mulungu, pamadza nthawi imene tiyenera kulola Mulungu kulankhula mwa ife mau ace angwiro.

B. Pamene nthawi yanu ya kulankhula za cikhulupiriro canu ku anthu ena yafika, kodi munganene ciani? Malembo athu mu Yohane atiuza ife zimene munthu wina analankhula.

"Nataniyeli anati kwa iye, ku Nazarete kutha kucokera kanthu kabwino kodi? Filipo ananena naye, tiye ukaone."

Filipo anakumana ndi Yesu ndipo anaitanidwa kumtsata. Coyamba anathamangira kukauza bwenzi lace Nataniyeli kuti apeza Mesiya, Mpulumutsi wolonjezedwa. Kwa zaka Ayuda anali kuyembekezera kudza kwa Mesiya. Nataniyeli anafunsa ngati kanthu kabwino kangacokere ku mzinda wa ung'ono monga Nazarete. Filipo anati tiye ukaone wekha.

Umboni wabwino siuli kawiri-kawiri m'ndandanda wa ziphunzitso, koma cimene Ambuye athu atanthauza kwa ife. Apanso ndi kukhudzidwa kwa munthu kumene kuli ndi phindu. Cinthu cimodzi coopsya kwambiri pa kucitira umboni ndi kufuna kutsutsa maganizo ena. Kutsutsana uku kumaononga nzeru za cikondi cimene tiyenera kukhala naco pa abwenzi athu. Nchito yathu ndi kufalitsa uthenga wabwino. Iyenera kukhala sankho ya winayo kukhulupirira kapena kusakhulupirira. Palibe munthu angatsutsane ndi zomwe wazimva ndi kuziona. Ndi zomwe za kucitikira ndi Mulungu ungaonetse cimene cimatanthauza kukhala Mkristu ndi cikondi cimene muli naco pa bwenzi.

Pamene muli kulankhula, Mulungu adzatsogolera mau anu ndi kugwira nchito mu mtima wa munthu amene sali Mkristu. Simuli nokha nthawi zonse pamene mucitira umboni mwa cikondi. Mulungu ali komweko pamodzi ndi inu.

Pamene moyo wanu ndi umboni wa moyo wanu mwa utsogoleri wa Mulungu satsegula khomo ku mtima wa munthu wina, ndime zocepekera zocoka M'buku Lopatulika zingathandize kuunikira njira ya Kristu. Pansipa pali ndime zocepekera zomwe zimaonetsa mwacidule njira ya Mulungu ya cipulumutso.

Aroma 3:23 - Anthu onse anacimwa ndipo ife tonse tifuna thandizo.

Yohane 14:6 Yesu ndiye njira ya kwa Mulungu.

Aroma 10:13 - Yesu anadza kupulumutsa aliyense.

Aroma 6:23 - Cipulumutso ndi mphatso, ndipo cimene muyenera kucita ndi kulandira mphatsoyi.

angakhale mlendo ku ena a abwenzi anu. Inu muli munthu woyenera kufotokozera bwenzi lanu kwa Mulungu.

Comalizira, tiri ndi lamulo kucokera m'Buku Lopatulika. Ambuye atiitana ife kufalitsa uthenga wa Yesu ndi kudzipereka nsembe kwace cifukwa ca ife kuli konse kumene tingapite. Tiwaphunzitse, kuwapanga ophunzira, ndi kuwalangiza malamulo a Mulungu. Ngati mudziwa Kristu monga Mpulumutsi, ndiye kuti muli ndi udindo wa kugawa za iye. Ndi pamene tipatsa Yesu ndiye pamene timudziwa bwino ife tomwe. Ngakhale koposa udindo mpata wa kugawira Kristu ndi mwai, ngati tiri ndi cakudya pamene ena ali ndi njala, tifuna kugawana ndi iwo. Si udindo cabe, ndi cisangalalo!

Ganizirani pa zifukwa za kugawira cikhulupiriro cathu. Pezani ndi pemphero ndi kuphunzira. Kumvetsetsa zifukwa za kucitira zimakonzekera anthu motani pa nchito yocitira umboni yokhayo.

## KODI TIMACITIRA UMBONI MOTANI?

A. Ngati mudziwa Yesu monga Mpulumutsi, muli mboni yace. Mu maganizo, sisankho yakuti mudzagawira cikhulupiriro canu. Muli mboni cifukwa ca umoyo umene mukhala. Mau athu onse sali okwanira ngati umoyo wathu siulodzera ena kwa Mulungu. Kuli mau akuti "sindingamve zomwe unena cifukwa ca phokoso limene ucita." Pali nthano ya anthu awiri, m'modzi nkhalamba ndi wina wa cinyamata, amene anali kupita mu mzinda ku kacitira umboni wa cikhulupiriro cao. Tsiku lonse anazungulira malo ocepa amalonda. Pamene nthawi ya m'madzulo inafika wa cinyamata anafunsa nthawi imene adzayamba kucitira umboni. Nkhalamba anaseka nati tinali kucita umboni tsiku lonseli. Ngati miyoyo yathu ionetsa cikondi ca Mulungu kwa ena, adzamva mau athu mokondwa. Ndi cinthu ca pafupi kwambiri munthu kukhulupirira kuti amukonda ndi kumsamalira ngati abwenzi ace Akristu aonetsa kale cikondi ndi kukhudziwa ndi munthuyo. Kodi moyo wanu ulodzera ena kwa Mulungu? Pokhapo ngati Kristu ali Mbuye wa miyoyo yathu, ndiye pamene ena adzapeza cithunzi-thunzi coona ca Mulungu kupyolera mwa ife. Ngati miyoyo yathu yaperekedwa ku utsogoleri wace, umboni wathu kwa iye udzakhala womveka koposa mau ali wonse amene ife tingalankhule, kapena ngakhale kukuwa pa tsindwi la nyumba. Tiyenera kucinjiriza miyoyo yathu kotero kuti umboni wace siudzakhala wocepekera pa cithunzi-thunzi coona ca Mulungu, mwini. Komatu, ngakhale pamene miyoyo yathu ili yoperekedwa



munthu amene ali ndi cingwe, ndipo wagwira cingwe kutipulumutsa ife. Kuti iye akhoze kutipulumutsa ife, komatu, tiyenera kutaya umoyo wathu wa ucimo ndi kuyamba kutenga cingwe, ndi kumpempha kutikokera kunja.

## YESU APULUMUTSA ALIYENSE

Palibe aliyense pa dziko lino lapansi ali wocimwitsitsa amene Yesu angalemphere kupulumutsa. Ngakhale dzenje la ucimo litalike motani la wina aliyense wa ife, ngati zoonadi tamva cisoni cifukwa cakusamvera Mulungu pa kucimwa, ndipo tifuna kupulumutsidwa, Yesu angatipulumutse. Ali wa mphamvu kutero. Mungazizwe m'mene munthu m'modzi, Yesu angapulumutsire anthu onse ndi imfa yace. Kumbukirani kuti Buku Lopatulika ikuti munthu aliyense ali wocimwa. Kodi iye akhoza motani? Yesu sanali munthu wamba. Ndi munthu yekhayo amene anakhala ndi moyo amene anali wopanda cimo. Anakhala umoyo wa ngwiro. Kumbukiraninso kuti Yesu anali mwana wa Mulungu. Mulungu anakonda mtundu wa anthu kotero kuti analola mwana wace, Yesu, kukhala munthu. Yesu pomwepo, anali munthu ndi Mulungu pamene anakhala ndi moyo pa dziko lapansi. Yesu analola yekha kuphedwa monga nsembe ya macimo onse a munthu. Ici ndiye cifukwa tikonda Yesu kwambiri; cifukwa anatifera ife.

## YESU ALINSO NDI MOYO

Pamene ophunzira ataika Yesu m'manda atapacikidwa, anadziwa kuti anali wakufa; ndipo anali acisoni. Ganizirani kuzizwa kwa pambuyo pa masiku atatu pamene anamva kuti Yesu wakhalanso wa moyo. Mwaona, imfa ndi mphoto ya ucimo. Mulungu sakhudzidwa ndi za imfa pa kuti Mulungu sacimwa. Kapena Yesu, koma pamene Yesu atabvomereza macimo pa iye, anayenera kufa. Komatu anali akali Mulungu, ndipo imfa siikanamugwirira. Tinena kuti anaukitsidwa. Anakhalanso ndi Mulungu, ndipo ngakhale izi zonse zinacitika pafupi-fupi zaka 2, 000 zapitazi, akali ndi moyo ngakhale tsopano, wokonzeka kukhulululukira macimo. Pamene Yesu wakhululukira ife macimo, pomwepo imfa siingakugwireninso. Tidzafabe, monga iye anacitira, komanso monga iye anacitira tidzauka ndi kukhalanso ndi moyo ..... koma coyamba tiyenera kumpempha kuti atipulumutse ife. Tikalibe mu dzenje, ndipo tiyenera kupemphera, kunena, "Yesu ndithandizeni." Ali wokonzeka ndi kuyembekezera kucita ici tsopano lino. Pamene tapempha thandizo lace, tiyenera

kumkhulupirira iye amene ali ndi mphamvu ya kutipulumutsa ife. Sicikuthandizani inu kukhulupirira kuti cingwe cidzakukokani kucoka mu dzenje ngati simukhulupirira munthu amene wagwira cingweco ndi kugwirako kucingwe iweyo kotero kuti akupulumutse.

Ngati iwe siuli Mkristu, Tsopano ndiye nthawi ya kukhala m'modzi. Ngati mukhulupirira Yesu angakupulumutseni inu, ndipo mufuna kutero, pomwepo gwetsani mutu wanu ndi kupemphera; Yesu, ndidziwa ndine wocimwa. Ndiri ndi cisoni posakumverani nthawi zapitazi. Conde mundikhululukire macimo anga, ndi kundipulumutsa ine. "Ndikhulupirira mungatero." Ndipo ngati zoonadi mukhulupirira, adzatero.

Pamene tacoka mu dzenje, tiyenera kuyamikira Mulungu pa kutipulumutsa ife. Tingatsimikize kuti watipulumutsa kwa muyaya. Koma ngakhale takhululukidwa macimo, ico sicitanthauza kuti tingapitirize kucita zoipa. Iye amene zoonadi wokhulupirira Yesu m'mtima wace adzafuna ku mpanga iye Mbuye wa moyo wace, osati cabe Mpulumutsi.

Umu ndiye m'mene mungakhalire Mkristu. Kodi inu ndinu Mkristu? Ngati sitero, zoonadi mudzaganizira pa za kukhala m'modzi wa Akristu. Kumbukirani ndinu wogwidwa mu dzenje la ucimo, ndipo Yesu ndiye njira yokha yoturukiramo.



Yesu amapulumutsa anthu a dziko lonse.





## KODI NDINGAGAWIRE BWANJI CIKHULUPIRIRO CANGA?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Yohane 1:41-46; Yesaya 55:10-11 Mateyu 28:19-20

**MAU A PA MTIMA:** *"Momwemo adzakhala mau anga amene aturuka mkamwa mwanga, sadzabwerera kwa ine cabe, koma adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira."* Yesaya 55:11

Nthawi zina mau angakhale a mphamvu kwambiri. Munthu amene angalankhule bwino ali munthu wa mphamvu kwambiri. Ngati mau ace angapange anthu kukhulupirira monga acitira kapena kucita monga afunira, munthu uyu ali ndi mphamvu.

M'mene timalankhulira kumauza anthu zambiri za ife. Tinadziwa anthu mbali ina cifukwa ca zimene amalankhula. Mau amene mugwiritsa nchito ali opambana. Angasinthe athu. Nthawi zina mau athu amalephera, koma Mulungu anatilonjeza ife kuti mau ace adzakwaniritsa colinga cao. Citsimikizo cathu ca cikulu mu kucitira umboni ku cikhulupiriro cathu ndi cakuti tiri ndi mphamvu kumbuyo kwathu ndi nzeru za Mulungu.

### 1. CIFUKWA CIMENE TIMACITIRA UMBONI Mateyu 28:19-20

Ngati Mulungu ali wa mphamvu motero, kodi ndi cifukwa ciani afuna ife kucitira umboni za iye? Kodi sangapulumutse amene afuna? Kodi sangatume cizindikiro ndi kucititsa aliyense kukhulupirira mwa iye? Awa ndiwo mafunso amene tiyenera kuyankha ngati tifuna kumvetsa cifukwa ciani Mulungu atifuna kufalitsa Mau ace. Kucokera pa ciyambi pa dziko lathu Mulungu wasankha anthu wamba kucita nchito yace. Mulungu afuna yense wa ife kuphunzira cimwemwe ca utumiki kwa iye ndi anthu anzathu. Ngakhale tiri ocimwa, Mulungu afuna ife kumudziwa iye mu utumiki. Yesu anati anadza kudzatumikira ena, osati kutumikiridwa. Mulungu amamvetsetsanso anthu cifukwa ndi mulengi. Ngati bwenzi labwino anakuuzani cinthu cina, mungamukhulupirire. Simungakhulupirire mlendo kapena munthu wina amene simudziwa bwino. Mulungu afuna kutigwiritsa nchito kufikira iwo amene tidziwa. Mulungu

## MPHATSO YA NTHAWI

Mulungu watipatsa ife nthawi. Kucokera pamene Mulungu analenga dziko. Anatilenga ife. Analenga nthawi. Kopanda iye, dzuwa silikanawala ndi dziko silikanatembenuka. Umoyo ndi wopangidwa ndi nthawi, igwiritseni nchito mwa nzeru kapena mopusa. Kodi Mulungu atiyembekezera ife kubwezera nthawi kwa iye motani? Kuli njira zambiri. Atiyembekezera ife kupatsa nthawi yathu yina mu mapemphero ndi kuphunzira Buku Lopatulika. Atiyembekezera kupatsa ina ya nthawi yathu pa kupita ku mpingo, ndiponso atiyembekezera kupatsa yina ya nthawi yathu pa kuuza ena za iye.

## MPHATSO YA MATALENTE

Ndimatalente otani amene muli nao? Kodi mungayimbire? Mulungu anakupatsani mauwo. Kodi mungalembe? Mulungu amakupatsani nzeru zanu. Ciri conse cimene mungacite, mu macicita cifukwa Mulungu yekha anakupatsani mphamvu ya kucita. Zinthu zimene mungakhoze kucita zichedwa matalente. Talente ili yonse imene muli nayo ndi yocokera ku mphatso ya Mulungu. Mulungu ayembekezera inu kuti mugwiritse nchito matalente ku ulemelero wace. Kodi inu mungacite bwanji tere? Ngati mu mayimba, imbirani Mulungu. Ngati mumaliza zilimba, muimbireni iye. Ciri conse comwe mungacite, ciciteni ku ulemelero wa Mulungu, ndipo adzakudalitsani inu cifukwa ca izo.





# KODI CIPEMBEDZO COONA NDI CITI?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Yohane 14:1-31

**MAU A PA MTIMA:** *"Yesu ananena naye, Ine ndine Njira, ndi Coonadi, ndi Moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine."* Yohane 14:6

Takhala tiri kulankhula pa za Cikristu monga cinali cipembedzo cokha, komanso ife tonse tidziwa kuli zipembedzo zina. Kapena mufuna kunena. "Nanga bwanji Cisilamu?" Kapena "bwanji milungu imene Asiya amapembedza, kapena milungu yakale ya Afrika?" Mungaziganizire "kuli milungu yambiri ndi cosatheka kudziwa cipembedzo coona." Ici siciri tero. Buku Lopatulika likuti tingadziwe cipembedzo coona. Tiyeni tiphunzire cipembedzo ciri conse pang'ono.

## MILUNGU YA KALE

Zaka zambiri zapita pafupi-fupi anthu onse amu Africa anali kupembedza milungu ya mitundu yao. Iyi milungu kawiri-kawiri inali zizindikiro za mphamvu ya cilengedwe.

Kunali mulungu wa mphezi, mulungu wa mvula, ndi tero. Uyu mtundu wa cipembedzo umachedwa "cipembedzo ca cilengedwe." Iyi milungu inapangidwa ndi anthu kucotsa mantha yao. Munthu anali kufuna-funa Mulungu, koma sanadziwe dzina lace kapena momwe angamfikire; motere milungu iyi, yosiyana kucokera ku mtundu ndi mtundu wina, amapangidwa. Onse anali kuyesetsa kumvetsetsa Mulungu woona. Munthu anali kuyesa kucepetsa kusiyana pakati ka iye ndi Mulungu.

## CIHINDU

Asiya ambiri ali acipembedzo cochedwa "Cihindu." Ici m'coonadi sicili cipembedzo cabe cimodzi, koma kusonkhanitsa zambiri pamodzi. Cimodzi-modzi monga mu Africa, zipembedzo za mitundu ndi mizinda zinayamba kupangidwa. Koma anthu anaona monga zipembedzo zonsezi ndi zosakwanira.

Anali kumva kuti kumalo ena kunali Mzimu umodzi "wogwirana umene iwo ndi cipembedzo cao anali gawo la iwo; motero anayamba kuika pamodzi zonse zipembedzo zing'ono kupanda cipembedzo cimodzi ca cikuru. Mtundu wa munthu anali akali kufunabe kufika kwa Mulungu, koma sadziwabe m'mene

angacitire. Iyi milungu inali yonse itatuluka pamodzi. Munthu anali kufuna Mulungu "wogwirana," Mulungu m'modzi.

**CIYUDA**

Bvuto linali lakuti munthu sakanakhoza kufika kwa Mulungu, koma Mulungu anayenera kufika pansi kwa Munthu, ndi kudzionetsera iye yekha kwa ife. Ici anacita ndi Ayuda. Ayuda achedwa "Anthu osankhidwa" cifukwa Mulungu anasankha kudzionetsera yekha kwa Abrahamu, pambuyo pace mwa lamulo imene anapatsa Mose, ndiyenso monga Mulungu amene tsiku lina adzadzionetsera yekha mokwanira kwa iwo pakutumiza mwana wace.

Uyu mwana anali Yesu Kristu. Ayuda ambiri sanakhulupirire kuti Yesu anali mwana wa Mulungu ndipo sanamulandire monga Mesiya amene Mulungu analonjeza. Ayuda ambili masiku ano akali kuyembekezerabe Mesiya kudza. Koma Ayuda ena anakhulupirira, ndi kupeza kuti Yesu Kristu anali ndi Mesiya amene mwa Iye lonjezo la Mulungu la kupulumutsa.dziko. Dziko lonse lakhala lirikuyesetsa kupyolera mu cipembedzo kufika kwa Mulungu, koma mwa Kristu. Mulungu amafika pansi kwa ife. Pamene tabvomereza Yesu Kristu monga Mpulumutsi wanthu ndi Mbuye, tacotsa cocinga pakati ka Mulungu ndi munthu cimene zipembedzo zina zayetsetsa kucotsa.

**CISILAMU**

Kulinso ena kucotsako Ayuda amene sadzakhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu. Muhamad anali munthu wotero. Anayamba cipembedzo codzika kuti cisilamu. Amuslimu apembedza Mulungu Atate m'modzi modzi monga yemwe Ayuda ndi Akristu amapembedza, ndipo amaganizira kuti Kristu anali mneneri wa mkulu. Ndi anthu odzipereka kwambiri, anthu abwino. Amuslimu amacita zinthu zonse zochulidwa mu mutu woti "kutumikira Mulungu." Ngati kucita zabwino kupulumutsa munthu, Amuslimu akanapulumutsidwa. Koma kucita zabwino sikungakupulumutseni inu. Cikhulupiriro cokha mwa Yesu Kristu monga mwana wa Mulungu. Ngati sakhulupirira kuti ali mpulumutsi wao, angawapulumutse bwanji? Yankho ndiya kuti sangakhoze pokhapo atakhulupirira.

**ZIPEMPEDZO ZINA**


Kuli zipembedzo zina zimene zimayesetsa kuika pamodzi zonse izi zipembedzo zimene tachula kukhala cipembedzo cimodzi cacikulu. Ici ndi cimodzi-modzi ndi comwe Ahindu amacita, apa



anagwiritsa nchito ndalama zace mosaganizira. Ngati siticita zimene Mulungu atiuza ife kucita, cipangitsa kukhala kobvuta kulankhula ndi Mulungu.

Monga Akristu, ca khumi cathu ndi ndalama yocepetsetsa imene tiyenera kubwezera kwa Mulungu. Mu Marko 12:43-44, Buku Lopatulika litiuza ife nkhani ya ndalama ya mkazi wa masiye. Yesu anali atakhala mu kacisi kuonerera anthu ali kuponya ndalama mosungiramo. Pamene mkazi uyu anadza, anaponyamo tundalama tiwiri mu cosungiramo. Sizinafike ngakhale ku muyeso wa 1 ngwee. Komatu, Yesu anati, ndithu ndinena ndi inu, mkazi wa masiye amene wa umphawi anaponya zambiri koposa onse a kuponya mosungiramo: Pakuti anaponyamo onse mwa zocuruka zao; koma iye anaponya mwa kusowa kwace zonse anali nazo, inde moyo wace wonse." Mark 12:43-44. Ngati mzimai uyu angapatse zonse zomwe anali nazo, zoonadi ifenso tingakwaniritse kupatsa ca khumi ca zonse zimene tiri nazo.

Cakhumi ndi cakhumi ca mphatso zonse za Mulungu. Kodi mphatso izi ndi ziti? Tiyeni tiyang'ane pa izo cimodzi-comodzi.



## MUTU 10

## KODI NDI CIFUKWA CIANI NDIYENERA KUPEREKA CA KHUMI?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Malaki 3:8-12, Marko 12:41-44

**MAU A PA MTIMA:** *"Mubwere nalo limodzi limodzi lonse lakhumi, kunyumba yosungiramo, kuti m'nyumba mwanga mukhale cakudya; ndipo mundiyese nako tsono, ati Yehova wamakamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndi kukutsamulirani mdalitso wakuti adzasoweka malo akuulandira."*
Malaki 3:10.

Mau a pa mtima alankhula za "cakhumi" kukhala ndi Ambuye. Kodi ca khumi ndi ciani? Ili ndilo funso tidzakambiranapo mu mutu uwu.

**CA KHUMI**

Mulungu afuna tibwezere kwa iye ca khumi ca zinthu zonse zimene watipatsa. Tiyeni tipatse fanizo la nthano. M' nyamata wa m' ng' ono anafuna kukaona kanema ndipo anapempha atate wace kuti amupatse ndalama. Atate wace anampatsa 50 ngwee, yokwanira kulipira ku kanema ndi ndalama yaswiti, koma anamuuza tsopano, mwana wanga, pamene wapatsidwa yotsalira ku 50 ngwee iyi, kumbukira kusunga 5 ngwee. Iyi ndi ndalama imene ungagwiritse nchito pa kunditumira lamya ndi kundidziwitsa kuti ufuna ndidzakutenge. "Pomwepo tate anacoka. M' nyamata uja wocepa anagwiritsa nchito gawo lina la ndalama ku kanema, ndipo anayamba kufuna zinthu zina, zinthu za 1 ngwee, mpaka anazindikira kuti anagwiritsa nchito ndalama zonse zimene anali nazo ndi kuti analibe ndalama ili yonse ya kutumira lamya atate wace. Anakhala pansi kulira mpaka anaona atafika. Pamene anali kulowa m' galimoto, tate wace anamuuza, "Waona! Ici ndico cimene cimacitika ngati siumvera atate wako."

Ndife olingana kwambiri ndi mnyamatayu. Mulungu watipatsa mphatso za zikuru zambiri ndi pempho lokha lakuti tibwezere limodzi la khumi la mphatso watipatsa. Mulungu analenga Golide ndi yahaloni (Daimondi). Safuna ndalama zathu, koma adziwa kuti tifunikira kupatsa. Ndi njira yathu ya "kugwirizana" ndi Mulungu. Ndi njira ya kuonetsa iye kuti timamukumbukira iye. Pamene sitipereka ca khumi, tikhala ngati mnyamata uja amene



tabwereranso kumbuyo komwe tacoka. Kodi ndi cipembedzo citi ciri coyenera? Amembala a cikhulupiriro ca Bahai, mwa citsanzo, akhulupirira kuti muli coonadi mu cipembedzo ciri conse. Mukufuna-funa coonadi ca cing' ono mu cipembedzo ciri conse, amasiya coonadi cacikuru ca Cikristu.

**CIPEMBEDZO COONADI**

Mulungu yekha ndiye angapange cipembedzo coona. Mtundu wa munthu sungakhoze. Cipembedzo cokha comwe Mulungu anapanga ndi Cikristu. Mukubvomereza kokha nsembe ya Kristu ya macimo athu ndiye pamene tingapulumutsidwe kwa iwo. Iyi ndiye njira imene Mulungu anakonzekera. Anafuna Cikristu kukhala cipembedzo coona. Ici ndiye cifukwa Yesu anati *"Ine ndine Njira, Coonadi ndi Moyo, palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa ine"* (Yohane 14:6).

# (PICTURE)



NDI KUPYOLERA MWA YESU YEKHA

## KODI NDINGATUMIKIRE MULUNGU MOTANI?

**MAU A PA MTIMA:** *"Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa Iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za pa dziko, ndi za pansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate."* Afilipi 2:9-11

Pambuyo pa kukhala Akristu tidzafuna kutumikira Mulungu. Onse timatumikira Mulungu pa kupanga Yesu kukhala Mbuyathu, monga mau athu a pa mtima anenera. "Mbuye" ndi wolamulira kapena mfumu. Ngati tipanga Yesu kukhala Mbuye wa miyoyo yathu, timulola kuti adzitipangira ife masankho. Kodi tingacite ici motani? Pali njira zisanu za kutumikira Mulungu.

**TUMIKIRANI MULUNGU PA KUPHUNZIRA ZA IYE**

Ngati muli ndi bwenzi, mufuna kudziwa za iye. Mufuna kudziwa dzina lace, kumene akhala, banja lace, ndi zinthu zina zimene zidzakuthandizani inu kumvetsetsa iye ndi mabvuto ace.

Pa nthawi imodzi mufunanso kumuuza za inu. Ici ndiye cokondweretsa coona ca ubwenzi. Mulungu afuna kukhala bwenzi lathu. Adziwa kale zonse za ife, koma afuna ife zocurukirapo zimene tingakhoze. Pali njira zambiri za kuphunzirira za Mulungu. Njira yabwino kopambana ndi kupyolera mu Buku Lopatulika. Buku Lopatulika ndi Mau a Mulungu; ndi Mulungu kulankhula kwa ife. Pamene tiwerenga Buku Lopatulika, timvera kwa Mulungu ali kulankhula, njira ina ya kuphunzirira za Mulungu ndi mwapemphero. Pamene tipemphera tilankhula kwa Mulungu. Kuphunzira Buku Lopatulika ndi kupemphera ku mapanga kulankhuzana ndi Mulungu. Kulibe njira yina ya kuphunzirira za bwenzi kuposa kulankhuzana. Njira ina imene timaphunzirira za bwenzi ndi pa kulankhula ku anthu ena amene amamudziwa. Kulankhula ku Akristu ena pa yekha pa yekha ndi njiranso yabwino ya kuphunzirira za Mulungu. Koma kumbukirani, nthawi zina anthu ali ndi uthenga wolakwika pa za bwenzi. Ena angakuuzeni cinthu cina pa za wina amene mudziwa cimene cingakusokonezeni inu. Ngati ici citacitika, mupite kwa bwenzi lanu pomwepo ndi kulankhula naye za comweco. Ici ndi cimodzi-modzi ndi Mulungu. Ngati munthu wina wakuuzani



onse owazungulira iwo. Kuti muyambe mpingo simuyenera kupanga mpingo wanu. Uyenera kukhala mpingo wa Mulungu, uyenera kumangidwa pa mwala wa cikondi ca Mulungu. Kudzakhala nthawi za mabvuto, pakuti Satana adzayambana ndi mpingo ndi mphamvu zace zonse. Cifukwa ife ndife anthu pa dzakhala kutsutsana. Komatu, mphamvu ya Mulungu idzakhalapobe. Yesu anati nyumba yomangindwa pa mcenga idzakokoloka ndi namondwe, koma nyumba yomangidwa pamwala idzakhoza kuimilira. Mpingo umangidwe pa mwala wokha wolimba, Mulungu wosasintha ndi wa muyaya. Kucokera ku ophunzira ocepa anamanga mpingo umene ufika ku dziko lonse. Ngati mumulola, ndi ciani cimene adzayamba kumene mukhala?

**1V. ZOKAMBIRANA**

Pezani mu Macitidwe zinthu zina zimene mpingo woyamba unacita, ndipo yesani tsopano kupeza ngati mpingo wanu ungakhoze kuzicita.

adzakhala acidwi. Ngati mwa inu aona monga ngati wina wodzadza mipando ndi kucurukitsa opezeka ku mpingo, adzaonanso izi. Mkristu pansi pa utsogoleri wa Mulungu adzapeza mipata yocuruka kuuza ena za mpingo uwu watsopano. Lolani Mulungu afalitse uthenga uwu mwa inu.

### 3. KODI MPINGO WANU UDZAKHALA MONGA CIANI?
Masalmo 55:4

Ndikukhudzidwa kwanu kumene kumacititsa anthu kufuna kudza ku mpingo, ndi kaonekedwe ka mpingo kumene kudzabweretsanso. Mu buku la Masalmo tiwerenga kuti mpingo uyenera kukhala malo a ciyanjano cabwino.

Ngati munalipo mu mpingo momwe mulibe amene anakulandirani kapena ku kupatsani moni, simungafune kubwererakonso. Ngati mpingo uli wodzadzidwa ndi cikondi ca Kristu, aliyense adzaona monga wolandiridwa komweko. Uyu mpingo watsopano siuyenera kukhala malo komwe anthu adzamva cisoni kapena womangika nthawi zonse. Mpingo woona wa Cikristu ndi malo a cisangalalo ceni-ceni. Yesu anacha kacisi mu Yerusalemu nyumba ya mapemphero. Uyu mpingo watsopano siuyenera kukhala malo komwe anthu adzamva cisoni kapena womangika nthawi zonse. Mpingo woona wa Cikristu ndi malo a cisangalalo ceni-ceni. Yesu anacha kacisi mu Yerusalemu nyumba ya mapemphero. Uyu mpingo watsopano uyenera kukhala malo otero, malo omwe anthu ali pafupi ndi Mulungu, kumene mudziwa monga bwenzi leni-leni. Pa mpingo uwu payenera kukhala maganizo akupezeka ndi utsogoleri wa Mulungu. Ophunzira anali kupempherera pamodzi pamene Mzimu Woyera anadza pa iwo. Lankhulani kawiri-kawiri ndi Mulungu pa za guru ili latsopano la okhulupirira. Pempidererani utsogoleri wace ndi mphamvu.

Pangani mpingo kukhala malo a ciyanjano. Pamene anthu atsopano abwera ku mapemphero, atengeko mbali ku zocitika. Afunseni kuti athandizire kuyendera, kuphunzitsa mu maphunziro a Buku Lopatulika, pa cikonzero ca zocitika, ndi kugawira zimene Kristu wa acitira. Anthu afuna kuthandiza. Afuna kukhala ciwalo ca guru. Abweretseni mkati ndi kuwathandiza kumva olandiridwa. Mu ciyanjano, cisangalalo, mapemphero, ndi ciyanjano zipanga mpingo uwu malo a cikondi, cikondi monga ca Mulungu. Ndi cikondi cimene Yesu anadza kudzatipatsa ife. Afuna mipingo yace kupatsa cikondi cotero ku



cinthu cina pa za Mulungu cimene cikusokonezani inu, pitani mukapeze coonadi kucokera kwa iye.

### KUTUMIKIRA MULUNGU PA KU BATIZIDWA

Yesu anabatizidwa mu mtsinje wa Yordano. Anacita ici kupatsa citsanzo ku onse omutsatira. Mu macitidwe 8 pamene mdindo wa ku Atiopiya amene Filipo ali kuuza za Yesu, anakhala Mkristu, anafuna kubatizidwa kuonetsa kwa ena kuti anali wotsatira wa Yesu. Kubatizidwa sikukupulumutsani. Yesu ndiye amene akupulumutsani kubatizidwa ndi cizindikiro ku ena ku zimene zacitika kale mu mtima wanu; kuti Yesu anatsuka macimo anu onse.

### TUMIKIRANI MULUNGU PA KUPITA KU MPINGO

Kawiri-kawiri pamene wina wabatizidwa akhala ciwalo ca mpingo. Ici ndi cabwino, pakuti Buku Lopatulika linena kuti, *"Kristu anakonda Eklesia, nadzipereka yekha m'malo mwace"* (Aefeso 5:25). Yesu anagwiritsa nchito nthawi yace pa dziko lapansi kukonzekera mpingo kufalitsa uthenga wa cikondi. Mu mpingo tiri ndi ciyanjano ndi Akristu ena, ndi aliyense mu mpingo alimbikitsidwa. Mulungu ali ndi malo mu mpingo ya Mkristu aliyense. Ngati mutapanga Yesu Mbuye wanu, mudzafuna kukwaniritsa malowa amene wakusungirani.

### TUMIKIRANI MULUNGU PA KUGAWIRA ENA CIKHULUPIRIRO CANU

Ngati muli ndi uthenga wabwino, simungayembekezere kuuzako ena za uthenga wabwino mu dziko lapansi lero ndi uthenga wa kuti Yesu Kristu anadza kudzatifera ife, ndi kuti tingapulumutsidwe mwa iye. Mkristu amene apanga Yesu Mbuye wa moyo wace adzafuna kuuza munthu aliyense kudziwa. Kumbukirani, ici ndiye cinthu comaliza cimene Yesu anatiuza kucita asanapite kumwamba. *"Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndi nakulamulirani inu; ndipo onani, ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimaliziro ca nthawi ya pansi pano."* Pamene nthawi ya pansi pano yafika ku mapeto ndi Yesu wabwereranso pa dziko lapansi mu ulemelero cinthu coyamba cimene adzafunsa abwenzi ace Akristu ndi cakuti "Kodi munacita zimene ndi nakuuzani inu kucita?" Ngati zoonadi tikonda Yesu, tidzauza ena za iye.

## TUMIKIRANI MULUNGU PA KUGAWIRA CUMA CANU

Mulungu watipatsa ife mphatso zambiri. Atifunsa kuti tibwezere zinthu zina kwa iye. Afuna nthawi yathu ina kukhala ya kutumikira iye. Popeza anatipatsa moyo, ndipo popanda iye sitikanakhala ndi nthawi konse. Afuna kuti ife tigwiritse nchito matalente athu kwa iye cifukwa zonse zimene tingacite iye ndiye anatipatsa mphamvu ya kucita.

Izi ndi njira za kutumikira Mulungu. Kucita zinthu izi sikudzakupulumutsani ngati simunabvomereze Yesu Kristu monga Mpulumutsi wa moyo wanu. M'mbali ina, ngati Kristu ndi Mpulumutsi wa moyo wanu, mudzafuna kucita zinthuzo zimene zimukondweretsa. Mau athu a pa mtima a phunziroli akuti tiyenera kubvomereza Yesu ndi milomo yathu. Koma kodi ngati macitidwe athu atsimikiza kuti lilime lathu linama? Kumbukirani, Mkristu abvomereza Kristu pamodzi ndi zicitidwe zacenso. Kodi inu munalola Yesu kukhala Mbuye wanu?





1. **KODI TIMACITA MOTANI?** Malemba mu Macitidwe 2:1-4

Kuli njira zambiri za kuyambiramo mpimgo. Komatu, zonse zilibe nchito popanda mphamvu ya Mulungu wa mphamvu yonse. Ophunzira anakumana mu cipinda cimodzi-modzi kumene anakumana kawiri-kawiri ndi Yesu. Anayembekezera mphamvu yace. Pamene anthu awa analandira mphamvu yace ya mzimu Woyera anapita kunja kukalalikira ndi kugwira nchito. Zonse zimene tingayembekezere ndi kugwiritsidwa nchito ndi mphamvu ya Mulungu mu kuyamba kwa mpingo. Ngati cacitika, cidzakhala kupyolera mu mphamvu zace mwa ife.

Tiyeni tiyelekeze tsopano kuti Mulungu wakutumani inu kunja kukagwira nchito mudela latsopano. Kodi ndi ciani cimene muyenera kucita?

Mipingo yoyamba inayambidwa m'manyumba. Pa nthawi ya kutsatira kuuka kwa Yesu guru la anthu amene anadziwika monga Akristu anacuruka mwamsanga. Paulo analemba makalata ku ena a mipingo iyi. Nthawi ndi nthawi analankhula za mpingo mu nyumba ya anthu ena. Ndipo pa kucinjiriza manyumba ang'ono ndipo mipingo inayamba.

Mipingo ikali kuyambidwa mu njira imodzi-modzi. Kuphunzira Buku Lopatulika kwa m'mawa pa tsiku la Mulungu m'nyumba kwina m'dela ndi njira yabwino ya kuyamba mpingo.

Mungaitane amene mukhala nao pafupi kudza ndi kukhala nao pamodzi mu maphunziro awa. Mu nthawi iyi, coonadi cacikulu ca cikondi ca Mulungu ali pafupi kuwamvetsa. Posacedwa mungakhale ndi oculuka mu nyumba. Tsopano mungafunse malo akulu. Guru nthawi zina siingakwanitse kumanga nyumba yopemphereramo, koma kuli malonso ena komwe angapite. Ku sukulu, mu manyumba amalonda omwe sagwiritsidwa nchito, ndi manyumba ena amene angakhale ndi malo akulu. Apanso citsogozo ca Mulungu cingaonetse njira. Cidziwitso ciyenera kukhala cofalitsidwa bwino mukakulidwe. Anthu ayenera kudziwa kuti pali mpingo. Kuyendela anthu mu manyumba ndi njira ya pafupi ndiponso yabwino. Kuitana ena kudza ndi kupembedza ndi kapena kucitira umboni wa cimene Yesu atanthauza kwa inu ungagwiritsidwe nchito kwambiri ndi Mulungu kubweretsa cidwi mwa bwenzi lanu. Mu mapepala ankhani kodi matiraki ndi kukumana pa za nchito kungapatse mpata wabwino wa kuuza ena za mpingo. Ngati anthu aona kuti muli ndi cidwi mwa iwo, ndi cisamaliro pa mabvuto awo,

## KODI MUNTHU ANGAYAMBE MPINGO MOTANI?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Macitidwe 2:1-4; Mateyu 7:24-27, Macitidwe 7:47-50

**MAU A PA MTIMA:** *"Ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo."* Mateyu 16:18b

Yesu nthawi zina ananena nkhani ya munthu amene ali kukonzekera kumanga nsanja. Munthu uyu anali wa nzeru. Akalibe kumanga anawerengeratu mtengo wa nchito. Anapeza ndi ndalama zingati zimene anali nazo ndiponso ndi ndalama zingati kumanga nyumba zonse zidzatenga. Kapena anayang'ana-yang'ana kuona ngati zipangizo anali kufuna zinali pafupi ndi kupeza anthu ogwira nchito. Munthu uyu wa nzeru sanafune kuyamba kugwira nchito ndi kupezeka kuti sangakhoze kumaliza. Tikalibe kuyamba mpingo tiyenera kucita cimodzi-modzi. Iyi ndi nchito imene tiyenera kucita cimodzi-modzi. Iyi ndi nchito imene tiyenera kupempherera. Tiyenera kuona za nthawi ndi zocita, ndi kupitirirapo. Khalani otsimikiza kuti tiri mu cifuniro ca Atate. Pamene tidziwa kuti ali ndi ife, pomwepo tiyambe nchito.

1. **KODI NDI CIANI CIMENE TIMAYAMBA?** Macitidwe 7:47-50

Kodi pa kuyamba mpingo mu mapita ndi kumanga nyumba yopemphereramo? Kodi ici ndiye mpingo? Malembo athu mu Buku la Macitidwe litiuza kuti Mulungu safuna nyumba ya kukhalamo, koma anthu amene adzamkonda iye. Yesu sanadze ndi kufera kuti ku kakhale manyumba okongola. Anadza ndi kufa kotero kuti munthu akhululukidwe ku macimo. Ndi anthu amene ali ofunikira kwa Mulungu! Mpingo umene anatuma mwana wace kuyamba ndi wopangidwa ndi anthu onse, osati njerwa kapena miyala. Mpingo wa Mulungu ndi anthu ace kuli konse kumene akumanako. Ali komweko pamodzi ndi ife pamene tikhala pamodzi kupembedza dzina lace. Muli malo ambiri mu mtima wa cikondi wa Mkristu kuposa mu nyumba ili yonse ngakhale ikule motani. Mpingo ndi anthu.





## NANGA ZA CIMO?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Genesis 3:1-13; Aroma 6:23

**MAU A PA MTIMA:** *"Pakuti mphoto yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu."* Aroma 6:23

Cimo ndi cinthu cimene tinamva kulankhulidwapo kwambiri. Ndi cinthu timadzíwa pa ife tokha. Imabweretsa cidani, nkhondo, ndi zonse zomwe ziri zoipa m'dziko. Timalica cimo, koma kodi ndi ciani? Kodi imacokera kuti? Kodi imacita ciani? Kodi tingaligonjetse? "Tidzayesa kuyankha mafunso onsewa pamene tiyankha funso la likulu," "Nanga za cimo?"

I. **KODI CIMO NDI CIANI?** Genesis 3:1-5

Ngati muli udzu m'munda wanu, simungodula cabe pamwamba pa udzu ndi mpeni. Mu maunyula kucotsa ndi midzu. Mbali imene simuona pamwamba pa nthaka ndiye yofunikira kwambiri. Uku ndi kumene zomera zimatengera cakudya cace. Macitidwe a ucimo mu dziko lathu sindiye cimo leni-leni. Komatu cimo ili ndi midzu yace m'mitima yathu.

Pamene Adamu ndi Hava anadya cipatso cimene Mulungu anawaletsa, cinali citsanzo cabe ca sankho imene iwo anacita. Mu ndime ya cinai: Buku Lopatulika litionetsa zimene njoka inanena kwa Hava cimene cinamucititsa kuti acimwe. Cinjoka cinauza Hava kuti Mulungu samukonda. Monga mwa cinjoka ngati Adamu ndi Hava adzadya za mtengo woletsedwawo, adzakhala ngati Mulungu. Adzakhala olingana ndi Mulungu. Pamene mwamuna uyu ndi mkazi anadya za mu mtengo, cinatanthauza kuti anali kuyesa kukhala milungu. Anali kutembenuka kucoka kwa Yehova Mulungu. Anali kusankha kulamulira miyoyo yao. Anacimwa! Ticimwa pamene tiganizira kuti tilingana ndi Mulungu ndi kusafuna kutsogolerewa. Sitimumvera iye cifukwa tikhulupirira kuti tingalamulire miyoyo yathu.

2. **KODI CIMO LICOKERA KUTI?**

Kodi mphatso yotani yaikulu koposa imene inu munalandirapo kucokera kwa bwenzi? Mulungu wa kupatsani inu mphatso yoposa. Pamene Hava anatenga cipatso ndi kupatsa Adamu, Mulungu sanawaletse. Tiri ndi ufulu wa kusankha kutsatira

kapena kusatsatira Mulungu. Nyama yocingiririidwa siingapite kumene ifuna kupita. Ilibe ufulu. Kodi ndimo m'mene Mulungu anatipangira ife? Iai, mphatso yaikulu imene Mulungu anatipatsa ife ndi ufulu wa kusankha pakati pa kutsatira lamulo lace ndi kutsata njira ya Satana.

*"Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m'maso, mtengo wolakalakika wa kupatsa nzeru, anatenga zipatso zace, nadya, napatsanso mwamuna wace amene ali naye, nadya iyenso."* Genesis 3:6

Kodi cimo la Hava linacokera kuti? Inacokera kusankho lace lomwelo. Cimo lathu limacokeranso ku sankho lathu. Mulungu atikonda ife kotero kuti sadzaticotsera ufulu wathu womutsatira iye kapena Satana; ngakhale kuti kawiri-kawiri timamukhumudwitsa pa kutenga njira ya ucimo. Anthu okhawo angalandire cidzudzulo ca macimo athu ndi ife eni. Ndife odzudzulidwa pa zonse zomwe cimo limabweretsa mu dziko.

### 3. KODI CIMO LIMABWERETSA CIANI?

Adamu ndi mkazi wace paciyambi anasangalala mu ciyanjano ndi ubwenzi wa Mulungu. Anakhala maola ambiri kulankhula ndi Mulungu. Anakondetsa Mulungu kwambiri. Cifukwa ciani tsopano anali kubisala kwa iye pamene anadza kudzawaona iwo? Anadziwa kucimwa kwao cifukwa ca kacitidwe ka kusamvera. Kucimwa uku kunawalekanitsa iwo kucoka kwa Mulungu. Pamene anaphunzira kudziwa cabwino kucoka ku coipa, anthu awa awiri oyamba anaona kuti anacimwa. Anadziwa nzeru imene cinjoka cinawalonjeza inawacotsa pamaso a Mulungu.

Cimodzi-modzi monga Adamu ndi Hava ifenso timacimwa masiku ano. Timayesa kutenga malo a Mulungu monga wolamulira miyoyo yathu. Zitsanzo za cimo ziri pali ponse tingayang'ane. Anthu akuda ena cifukwa cikumba cao ciri cosiyana ndi cao. Cidani ici cimatsogoza ku nkhondo cimene cimaonjezera kutipatula kucoka kwa Mulungu. Anthu sangakhoze kuyang'ana pa kucimwa kwao motero amaledzera kuti ayiwale khalidwe lao. Anthu awa amabisala kwa Mulungu cimodzi-modzi monga Adamu ndi Hava anacitira. Zonse izi ndi zina zocurukirapo zocokera ku khalidwe mu miyoyo yathu imene imacititsa ife kusamumvera. Comalidzira, cimo limabweretsa imfa idzatigonjetsa ngati cimo ndiye Mbuye wathu.



Cikhulupiriro mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wa moyo wace, kukhala wokonzeka kukhala kapolo kwa onse, mboni yopanda cirema. Cingaoneke monga izi zofunikira ndi zobvuta kwambiri kwa kuti palibe amene angakwaniritse kukhala mbusa, koma tiyenera kukumbukira kuti Yesu analonjeza kutithandiza ife kukhala munthu wabwino. Akaitana munthu kukhala mbusa, adzampatsa iye mphamvu zokwanira ndi nzeru mwa pemphero ndi kuphunzira Buku Lopatulika. Koma monga mu mbali zina za utumiki wa Cikristu, iye amene adzakhala mbusa ayenera kusamila pa Yesu Kristu. Ciyembekezero cathu cokha ndi Yesu.



ayenera kukhala ngati sing'anga wa zosowa za uzimu za munthu. Ayenera kukhala wokonzeka kuutsidwa pakati pa usiku kuthandizira iwo amene ali ndi mabvuto. Ici ndiye cimene Yesu anatanthauza pamene ananena kuti tiyenera kukhala akapolo.

**ZOFUNIKIRA**

Pamene Paulo, mtumwi wochuka, analemba poyamba-yamba kwa Timoteo, anali ndi zinthu zambiri zonena pa zofunikira kukhala mbusa. Tiyeni tiyang'ane pa zinthuzo: Mbusa ayenera akhale wopanda cirema. Ici citanthauza kuti ayenera kukhala umoyo wabwino wakuti palibe amene angamuneneze zoipa. Ayenera kukhala ndi mkazi m'modzi, wodzisunga, ndiye kuti ayenera kukhala wa maganizo abwino, wodzilemekeza, wokonda kucereza alendo, wosakhumba cuma. Izi zonse ndi magawo akusapanda cirema. Ngati munthu ali ndi zinthu izi nthawi zonse, palibe zambiri zimene munthu aliyense angalankhule pa za iye zimene zingakhale zoipa.

Mbusa ali ndi nchito yobvuta kwa kuti ayenera kutsogolera mpingo umene upangidwa ndi anthu, angakhale ndi Akristu, nthawi zina ali ndi mkangano woipa. Paulo anena kuti mbusa ayenera kukhala wolimba kuweruza banja lace la iye mwini, cifukwa ngati sangatero, adzasunga bwanji mpingo wa Mulungu? Monga mbusa adzakumana ndi mabvuto ocuruka oposa omwe amapezeka mu banja liri lonse. Mbusa ayenera kukhala munthu amene angakhoze kugonjetsa mabvuto awa.

Mbusa sayenera kukhala Mkristu watsopano. Ici ndi capafupi kumvetsetsa. Ngati munthu wangophunzira za Yesu iye mwini, angaphunzitse ena bwanji zinthu zimene sanaphunzire bwino? Ndi cinthu cabwino kwa Mkristu watsopano kukhala wolonzeka kutumikira Mulungu monga mbusa, koma coyamba ayenera kuphunzira zambiri angakhoze za Buku Lopatulika ndi "kulimba mwa Ambuye."

Mbusa ayenera kukhala munthu wolemekezeka ku onse akunja ndi Akristu omwe mu mudzi wa kwao. Pakuti ngati wakunja salemekeza mbusa amene amuuza iye za Kristu, adzakhala ndi maganizo ozifunsa kodi zoonadi adzalemekeza Yesu iye mwini.

Mbusa ayenera kupitiriza kukhala mboni yabwino, osati zimene anena zokha, komanso mu zimene acita.

Izi ndiye zofunikira zimene zimapanga mbusa wabwino:



Cimo ndiye cinthu cokhaco cimene cimakwiyitsa Mulungu. Imatilekanitsa ife ndi iye. Imatipangitsa ife kuda mbale wathu. Imatipereka ife ku imfa.

1V. **KODI TINGACITE CIANI ZA IMFA?** Aroma 6:23

*"Pakuti mphoto yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu."*

Mphoto ndi cinthu cimene timalandira titagwira nchito. Pambuyo pakugwira nchito yolimba tsiku lonse tiyembekezera malipiro kapena mphoto. Cifukwa ca macimo athu ife anthu talandira imfa imene tiyenera kulandira cilango. Pamodzi ndi imfa zikudza zotsatira zina za cimo monga zomwe tachula. Cimo ili ndi la mphamvu kutipambana ife. Tioneka nthawi zonse kutsutsana ndi kucimwira Mulungu. Kodi cimene cimatipangitsa ife kucimwa nthawi zonse ndi ciani? Ndiye citsanzo cabwino kopasa ca zanthu zonse zotsutsana naye Mulungu ndi Satana. Kodi munamva kale cinthu cina ca kukuuzani kucita zinthu zimene mudziwa kuti ndi zolakwika? Iyi ndi nchito ya Satana mwa inu! Ali wa nzeru kwambiri ndi wa mphamvu kwa ife. Cioneka monga kuti kuyenera kucimwa ndi kufa nthawi zonse. Komatu, zotsalira za Aroma 6:23 litilodzera ife ku njira yakuti mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha. Simugwirira nchito mphatso. Mphatso ndi cinthu cimene cimapatsidwa kwa inu mwaulere. Ndi mphatso ya moyo wosatha, osati imfa yocokera ku cimo. Pakuti Mulungu angagonjetse kutsutsana naye kumene kuli mwa iye. Mphamvu yace ingakucotse mu miyoyo yathu ndi kubweretsa moyo wa muyaya ndi iye. Sitingayenere moyowu, koma tingaulandire kuti ukhale wathu kucokera kwa Yesu Kristu. Mkristu ndi munthu amene wadzipereka yekha kwa Yesu kotero kuti angagonjetse cimo mwa iye. Ndipo imfa yace pa mtanda Yesu analipira ngongole imene tinali nalo kwa Mulungu. Anafa m'malo mwathu, kotero kuti mphatso ya moyo ingapatsidwe kwa inu!


Adamu ndi Hava anasankha kusamvera Mulungu ndi kulandira cilango. Komatu, mungasankhe kucotsa macimo anu onse, ndi kutenga Yesu kukhala mfumu ndi kulandira mphatso imene analonjeza moyo pamodzi ndi iye nthawi zonse. Monga cimo ndi kutsutsana ndi Mulungu, cipulumutso ndi kudzipereka. Kudzipereka kwanu kwa Mulungu kungagonjetse cimo.

**MAFUNSO YA KUKAMBIRANA:**

1. Ngati Yesu analipira ngongole ya macimo athu, kodi ndi cifukwa ciani yakalibe kukhululukidwa?

2. Kodi ndi m'njira zotani zimene Satana alankhula kwa inu?

3. Ngati tibvomereza Kristu koma ticimwira cimwirabe nthawi zina, kodi ici citanthauza kuti Satana ali ndi mphamvu zambiri koposa Mulungu?







## KODI ANGAKHALE MBUSA NDANI?

**MAU A PA MTIMA:** *"Ndipo m'mene anakhala pansi anaitana khumi ndi awiriwo; nanena nao, ngati munthu afuna kukhala woyamba, akhale wakuthungo wa onse, ndi mtumiki wa onse."*
Marko 9:35

**PHUNZIRO:** 1 Timoteo 3:1-7

Mu phunziroli tidzakambirana za mbusa. Mbusa, kapena woyang'anira monga amachulidwa nthawi zina mu Buku Lopatulika, ayenera kukhala kapolo wa mpingo wonse.


**MKRISTU NDI MAITANIDWE**

Ndithudi, cinthu coyamba cofunikira kwa mbusa ndi cakuti ayenera kukhala Mkristu. Ici cingaoneke kuti ciyenera kukhala tero ndipo mungazizwe cifukwa ndi ciani tiri kucichula, koma mwatsoka pali ena amene afuna kukhala abusa a mpingo amene sadziwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wao. Kapena amaganizira kuti kukhala mbusa kudzawapatsa mphamvu. Koma pakuti imodzi ya nchito yaikulu ya mbusa ndi kuuza ena za Yesu, ayenera coyamba kukhala Mkristu iye mwini. Yesu afuna Akristu onse kuuza ena za iye, koma safuna onse kukhala abusa. Munthu akalibe kuganizira kuti afuna kukhala mbusa, ayenera kufuna utsogoleri wa Mzimu Woyera mwa pemphero ndi kuwerenga Buku Lopatulika. Ngati akumva zoonadi kuti Mulungu afuna iye akhale mbusa, pomwepo timati "anaitanidwa ndi Mulungu" kucita nchitoyi. Munthu asayetse kukhala mbusa ngati sanaitanidwe ndi Mulungu.

**KAPOLO WODZIPEREKA**

Mbusa ali ndi nchito zambiri. Kucotsako kulalikira za Yesu kwa amene samudziwa, mbusa ayeneranso kuthandizira mamembala a mpingo kudza pafupi ndi Mulungu. Ayenera kuyendera iwo amene sabwera ku mpingo ndi kuwaitana kuti abwere. Ayenera kucezera odwala a mu mpingo wace ndi kukhala wokonzeka kupereka mphamvu ya Mulungu mu nthawi ya cisoni ndi imfa. Ayenera kukhala wokonzekera kuthandizira aliyese amene adza kwa iye ndi bvuto limene lifunikira thandizo. Ayenera kukhala mphuzitsi wabwino. Pali zinthu zocepekera zokha zimene mbusa ayenera kukhala wokonzeka kuzicita. Mu coonadi, kukhala mbusa ndi nchito ya kukhala pa nchito nthawi zonse. Mbusa

munthu wotero. Mtsogoleri wathu Yesu Kristu afuna anthu otsogolera Akristu ace. Aitana akapolo amene afuna kutumikira Mulungu wao ndi kuonetsa cikondi cace ku anthu onse. Kodi Mulungu angakutengeni kuti mukhale munthu wotero?



M'BUSA OZIPELEKA KAPENA M'TUMIKI AMAPHUNZIRA KU M'PINGO WACE.

**(Mbusa kapena Mtumiki wodzipereka)**





## KODI ANGAKHALE MEMBALA WA MPINGO NDANI?

**MAU A PA MTIMA:** *"Cotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi mkulimba kwa mphamvu yace."* Aefeso 6:10

Lero tidzakambirana funso "Kodi angakhale membala wa mpingo ndani?" Buku Lopatulika linena kuti Yesu akonda mpingo cimodzi-modzi monga mwanuna ayenera kukonda mkazi wace. Ngati Mpulumutsi wathu aganizira kuti mpingo uli wofunikira motero, ifenso tiyenera kukhulupirira tero, ndi kuthandizira mpingo kukula.

### KODI MPINGO NDI CIANI?

Mpingo ndi guru la anthu obatizidwa okhulupirira mwa Yesu Kristu. Kuti mukhale membala wa guru la mpingo, munthu ayenera coyamba kukhala Mkristu, wokhulupirira. Ndiye pomwe angakhale membala mwa ubatizo. Ndi citsanzo ca kunja ca kusinthika kwa mkati, ndiponso ndi citsanzo cimene mpingo umabvomereza mu ciyanjano. Motero mungaone kuti ubatizo ndi umembala wa mpingo ndi zogwirizana pamodzi.

### KULOWA MU CIYANJANO

Ngati tikumbukira kuti ubatizo siutipulumutsa ife, koma m'malo mwace uli njira yakuonetsa ena kuti ndife Akristu ndi kulowa mu ciyanjano ca mpingo, pomwepo tingamvetsetse cifukwa ciani mpingo uyenera kusankha anthu awo amene adzakhala mamembala. Guru la mpingo silifuna anthu monga mamembala amene akuba ndi kunama ndi kunyenga ena kapena amene amacimwa mu njira zina pamaso pa anthu onse. Ngati munthu zoonadi akonda Yesu, adzatembenuka zoonadi ku macimo ace a kale. Ngati muli anthu mu mpingo amene kawiri-kawiri amatembenukira Mulungu, pomwepo ena kumene mukhala sadzaganizira zabwino za mpingowo. Sadzakhulupirira kuti Yesu ali kugwira nchito mwa iwo. Motero mpingo uyenera kusamala kulola okhawo mu ciyanjano cace amene anatembenuka kusiya zoipa zao.

Uku sikunena kuti mpingo siuyenera kukhala pamodzi ndi ocimwa. Yesu anati ndinadza kudzapulumutsa ocimwa, ndipo ndi ku munthu wocimwa kumene mamembala wa mpingo ayenera kuuza nkhani ya Yesu Kristu. Koma kuti wocimwa akhale

wololedwa kukhala membala mu mpingo, ayenera kulapa macimo ace.

**KODI MPINGO UMACITA CIANI?**

Pakuti mpingo ndi ciyanjano ca mamembala a mpingo, tingakambirane nchito ya mpingo monga nchito ya mamembala onse. Coyamba mpingo uli ndi nchito ya kupata osapulumutsidwa kwa Kristu. Yesu anatiuza ife tonse "cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la mwana, ndi la Mzimu Woyera." Tingacite ici pokhapo titagawira Yesu Kristu kuli konse kumene ife tipita. Koma ici sindico cokha ca lamulo lalikuru. Ipitiriza "ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu." Iyi ndiyo nchito yaciwiri ya mpingo, kuphunzitsa ndi kuzoloweza Akristu mu m'mene angatumikire Yesu bwino.

**KUTUMIKIRA MULUNGU**

Ngakhale pambuyo pa kukhala Mkristu, mayesero a kucimwa amakhalabe olimba. Ali olimba kwambiri, m'coonadi, kuti mphamvu yekha ya Yesu ingakhoze kuikaniza. Motero Akristu ayenera kuthandizana wina ndi mnzace kudza kufupi ndi Kristu. Mpingo ndiwo malo abwino kopambana ndi okumanilanapo Akristu ndi kupembedza Mulungu, ndi kudza pafupi ndi iye. Mwa kuyimba zomuyamika iye, mwa mapemphero, mwa kuphunzira malembo ace ndi mwa kumvera ku ulaliki, Akristu amapereka nzeru zao kwa Mulungu ndi kukhala kutali ndi cimo. Iyi ndi njira yokha ya kugonjetsera Satana. Ngati nzeru zathu ziri pa Mulungu, mayesero akulu adzaoneka opanda tanthauzo ndipo adzagonjetsedwa.

Koma kuli nthawi pamene ife tonse timalakwitsa. Ngati membala wacita cimo, mamembala ena a mpingo ayenera kucita zotheka kumuthandizira kulizindikira ndi kulicotsa m'moyo wace. Pokhapo atalapa cimo lace, ndiye pamene angaone kuti ali wolungamitsidwa ndi Mulungu. Cinthu coipitsitsa Mkristu mnzako angacite ku munthu ndi kumutembenukira kumupewa cifukwa ca cimo lace. Ife tonse ndife ocimwa, koma Yesu adzakhululukira munthu aliyense amene alapa ndi kupempha cikhululukiro. Mkristu ayenera kukhala wokonzeka kukonda nthawi zonse ndi kukhululukira wocimwa, monga momwe Yesu aliri.



kugwiriziza mu nthawi ya ciombolo. cikhulupiriro ici cimadza ndi kukula cokha mwa Cikristu cifukwa mtumiki ayenera kukhala ndiye amene anayesedwa ndi kupezeka woyenera ndi wolimba. Simungatenge munthu aliyense amene mukumana naye pa njira ndi kumpanga kukhala wolamulira dziko lanu lonse. Anthu ocepekera okha angakhoze kucita nchitoyi. Osati munthu aliyense angakhale Stefano kapena Filipo wina. Munthu wotero ayenera kuti anaonetsa kucenjera kwace ndi kudzipereka kwace kupyolera m'kutumikira mu mpingo. Cinganenedwe kuti mtumiki ayenera kukhala Mkristu weni-weni mu mau ndi m'kutumikira. Ayenera kukhala munthu wokhulupirika, wodzisunga, wa cikhulupiriro colimba, ndi ca mphamvu cimene cinayesedwa ndi kupezeka wodalira mu cikhulupiriro mwa Yesu Kristu.

**111. NCHITO YA MTUMIKI**

Ngakhale kuti atumiki oyamba anasankhidwa kutumikira osauka, iyi siinali nchito yao yokha. Anali anthu a Mulungu odzipereka amene anafalitsa mau monga ophunzira oona.

Malembo athu atiuza za kucitira umboni wa ophunzira. Stefano, kapena wodziwika kwambiri wa atumiki oyamba, anaponyedwa miyala mpaka kufa cifukwa analankhula mau a za Yesu mokhulupiririka kuti monga Mwana wa Mulungu. Filipo anatsogozedwa ndi mzimu kucipululu. Komweko anakomana ndi kulankhula ndi msungi cuma wa mfumu ya ikazi ya ku Atiopiya (tsopano Saudi Arabiya). Uyu anali munthu wa mphamvu zambiri amene anakumana ndi Filipo mu mphepete mwa njira. Anali munthu anali kufuna-funa Mulungu. Anali mtumiki Filipo amene Mulungu anagwiritsa nchito kutumiza nkhani ya Yesu mu dziko la tsopano. mtumiki uyu anali mboni. Monga atsogoleri a mpingo atumiki ayenera kuthandizira mbusa ndi kumthandiza kufalitsa uthenga wa bwino wa Yesu Kristu. Anthu awa ayenera kukhala amene athandiza mbusa kutsogolera mpingo. Ngati ali omasuka ku maitanidwe a Mulungu, angagwiritsidwe nchito kwa kukulu ndi Mulungu m'kutsogolera anthu a Mulungu. Pamene mpingo ulibe mbusa, ochuka a asilikari ndi iwo anali ndi owatsatira olimba. Anali anthu amene akanakhoza kutsatira malamulo ndi kugwiritsa nchito malamulowa pamene anali kufunikira. Anali anthu olimba mtima ndi omvera. Anali anthu amene akananyamula zolema za udindo. Mtumiki ayenera kukhala

## 11. **UMOYO WA MTUMIKI** 1 Timoteo 3:8-13


Kodi mtumiki ayenera kukhala munthu wotani? Ayenera coyamba kukhala wokhulupirika. Atumiki ayamba nchito yao pa nthawi imene Akristu ena anali kupasidwa milandu ya kusakhulupirika. Cinali kunenedwa kuti ena osauka anali kuiwalidwa. Ophunzira anadziwa kuti akapolo atsopano adzakhala oyang'aniridwa mosamala. Ayenera kukhala anthu amene palibe munthu aliyense adzakaikira kukhulupirika kwao. Masiku ano kukhulupirika ndi muyeso umene anthu amayesedwa nao. Munthu wokhulupirika amasiliridwa, koma wosakhulupirika sakhulupiridwa ndi aliyense. Pakuti mtumiki adziwika monga Mkristu ndi mtsogoleri wa mpingo, ayenera kukhala munthu wokhulupirika ndi onse. Buku Lopatulikanso likuti mtumiki asakhale womwetsa vinyo. Munthu aliyense amene ataya nthawi yace mu bawa sadzakhala ndi nthawi ya kutumikira Mulungu kapena kuthandiza munthu mu nzace. Munthu woledzera sangaziletse yekha. Ndani adziwa zimene adzacita pamene ali woledzera? Kodi citsanzo ca Cikristu cotani cimene angapatse munthu woledzera? Munthu amene ali ndi Yesu mu mtima wace safunikira kuiwala mabvuto ace ndi botolo, cifukwa Yesu afuna kuthetsa bvuto lace. Iai, mtumiki sayenera kukhala cidakwa. Cimwemwe cace ndi malo acicinjirizo ayenera kukhala mu ciyanjano ndi mbuye woukitsidwayo.

Mtumiki ndi muntu wacikhulupiriro. Buku Lopatulika likuti ayenera kukhulupirira "cisinsi ca cikhulupiriro mcikumbu mtima coona?" Cimodzi-modzi monga nchito inali yolimba kwa Mose ndi ophunzira, idzakhalanso yobvuta ku mtumiki. Kudzakhala mabvuto ambiri amene adzakumana nao tsiku ndi tsiku. Ngati sagwiritsa cikhulupiriro cace mwa mphamvu ya Mulungu kugonjetsa mabvuto akulu-akulu, kudela nkhawa kwace kudzacipanga colimba kwa ifye kukhala kapolo wokhulupiririka. Munthu amene ataya cikhulupiriro cace mu nthawi ya mabvuto sali woyenera nchitoyi. Satana adzagwiritsa nchito mphamvu zace zonse kutifoketsa ife. Adzamenyana ndi ife koma Satana sadzapambana. Mulungu adzagonjetsa. Ndi ciyembekedzo comweci cimene ciyenera kukhala pansi pa mtima pa munthu woitanidwa kukhala mtumiki. Ayenera kusunga cikhulupiriro cace pamene ena ataya cikhulupiriro cao. Munthu sangaone m'mbanda kuca umene sungagonjetse mdima. Mtumiki ayenera




## **ZIDA ZA MKRISTU**

Phunziro lathu la lero licokera mu Aefeso 6 ndipo lilankhula pa za zida membala wa mpingo wa Cikristu ayenera kubvala kuti aime ndi kumenyana ndi Satana. Zigawo za zida zimene Paulo achula ndi zinthu zabwino ku membala aliyense wa mpingo kuzifuna. Tiyeni tiziyang'ane cimodzi ndi cimodzi.




Coyamba mtumwi Paulo atilimbikitsa ife kudzimangira m'cuuno wathu coonadi. Coonadi ici ndi cakuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu, kuti anadza kudzatipulumutsa ife, ndi kuti pa kubvomereza iye tipulumuka. Caciwiri, tiyenera kukhala ndi ca pacifuwa ca cilungamo pa mtima wathu. Cilungamo ndi kukhala ndi cilimbiko ca kucita cimene ciri colungama. Pa nthawi ili yonse, ngakhale muopsyesedwe motani kapena muyesedwe motani. Cotsatira, Paulo akuti mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a uthenga wabwino wa mtendere. Kopanda nsapato, msilikali sangapite kuli konse, monga ife Akristu sitingapite kuli konse kapena kukhala aphindu ili lonse popanda kudalira pa uthenga wabwino wa Yesu Kristu monga umapatsidwa mu Buku Lopatulika. Cacinai, Paulo achula cikopa

ca cikhulupiriro; kopanda cikopa ca kudzicinjiriza naco, msilikali angakhale muciopsyezo cacikulu. Cimodzi-modzi, Mkristu ayenera kukhala wocinjirizidwa ndi cikopa ca cikhulupiriro mwa Yesu Kristu. Ndipo pamenepo kuli cisoti ca cipulumutso, cipulumutso cimene cimadza kucokera kwa Yesu yekha, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu (Buku Lopatulika). Ndi zinthu izi msilikali wa Cikristu ali wokonzeka kumenyana nkhondo ndi cimo ndi zoipa.



Kugawira Yesu ndi ena, kudza pafupi ndi Mulungu, ndi kumenyana nkhondo ndi ucimo kuli konse kumene ungadzionetsere okha ndi nchito ya membala aliyense wa mpingo. Koma sitiyenera kufoketsedwa, pakuti Yesu Kristu iye mwini anati, mu ndime yomaliza ya lamulo lalikulu, *"Ndipo onani, ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimaliziro ca nthawi ya pansi pano"* (Mateyu 28:20).





## KODI NDANI ANGAKHALE MTUMIKI?

**KUWERENGA KWA MALEMBA:** Macitidwe 6:1-6; 8:26-40; 1 Timoteo 3:8-13

**MAU A PA MTIMA:** *"Pakuti iwo akutumikira bwino adzitengera okha mbiri yabwino, ndi kulimbika kwakukuru m'cikhulupiriro ca mwa Kristu Yesu."* 1 Timoteo 3:13

Mu mutu wa 18 wa Eskodo timawerenga za nkhani ya mtsogoleri wotopa. Mose anatsogolera anthu a Israyeli kucoka mu Igupto. Anaona mphamvu ya Mulungu pa nyanja yofiira, ndi utsogoleri wa Mulungu mwa moto ndi utsi. Akanakhoza kutsogolera anthu awa ocuruka koma sakanakhoza kukhala pamaso pa anthu kuwathandizira kuthetsa mikangano yao ing'ono-ing'ono ndi kukhala ngati wobweretsa mtendere, koma anali oculuka. Nchito inamkulira kwambiri. Posacedwa mpongozi wace Yetero anabweretsa ganizo yakuti asankhe atsogoleri womuthandiza nchito. Palibe mbusa angacite nchito yace pa yekha. Afunikira thandizo locokera ku Akristu odzipereka. Pakati pa atsogoleri pali atumiki.

### 1. ATUMIKI OYAMBA

Panali madandaulo mu mpingo watsopano mu Yerusalemu. Ena anaona monga kagawidwe ka zinthu ku osauka ndi amasiye sikunali kucitika molinganiza. Ophunzira a Yesu anali kucita nchitoyi. Komatu, nchito yao inali ya kulalikira ndi kuphunzitsa kunapangitsa kukhala cobvuto kuyang'ana zosowa zonse za Akristu. Pambuyo pakuitana mpingo pamodzi, anaganizira kuti amuna asankhidwe monga atsogoleri woona a mpingo, amuna okhulupirika ndi odzipereka ku utumiki wa Kristu. Amuna asanu ndi awiri otere anasankhidwa. Mpingo watsopano unakhala ndi atumiki ace oyamba. Nchito yao siinali yopepuka ndipo siinabweretse ulemelero kapena ciyamiko cacikuru. Koma utumiki wao unali woona. Mpingo wa Mulungu masiku ano ufunikira anthu otero a cikhulupiriro ndi mzimu wakugwira nchito ndi mphamvu. Yesu afuna-funa amuna monga awa kugwira nchito m'munda, kututa, kusamalira, ndi kukonda miyoyo ya anthu.